# Baibulo ndi Buku Lochokera kwa Mulungu (Gawo 1)

Nkhaniyi yachokera m'buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* mutu 2. Bukuli likupezekanso pa jw.org.

**ZIMENE MUYENERA KUCHITA:** Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, komanso onani zimene zingakuthandizeni kufotokozera ena zimene mumakhulupirirazo.

## KODI BAIBULO LINACHOKERADI KWA MULUNGU?

### 1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N'chifukwa chiyani ena angayankhe kuti ayi? .....

.....

N'chifukwa chiyani ena angayankhe kuti inde? .....

.....

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

.....

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo? .....

.....



www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

## 2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

**Mulungu anauza anthu kulemba zimene zili m’Baibulo.**
(Werengani mutu 2 m’buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 1 mpaka 5.)

### Werengani 2 Timoteyo 3:16 ndi 2 Petulo 1:21.

Kodi muganiza kuti Baibulo limatanthauza chiyani likamati anthu amene analemba Baibulo “analankhula mawu ochokera kwa Mulungu”?

.....

.....

.....

Kodi mungagwiritsire ntchito chitsanzo chotani, pofuna kusonyeza kuti anthu omwe analemba Baibulo, ankalemba zimene Yehova anawauza osati za m’maganizo mwawo?

.....

.....

.....

**Bwana angauze sekilitale wake kuti alembe kalata, koma uthenga wa m’kalatayo ungachokere kwa bwanayo. Mofanana ndi zimenezi, anthu analemba Baibulo koma uthenga wake unachokera kwa Mulungu**


www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

## Baibulo ndi lolondola pa nkhani ya sayansi ndi mbiri yakale.

(Werengani mutu 2 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 6 mpaka 9.)

### Werengani Yobu 26:7 ndi Yesaya 40:22.

Kodi malembawa akusonyeza bwanji kuti Baibulo lili ndi mfundo zimene zinali zotsogola pa nthawi imene linkalembadwa?

.....

.....

.....

### Werengani Numeri 20:2-12.

Kodi mukuona kuti zinali zophweka kuti Mose alembe zolakwa zake m'Baibulo? N'chifukwa chiyani mukuganiza choncho?

.....

.....

.....

Kodi ndi ulosi uti wa m'Baibulo umene **umakuchititsani** chidwi?

.....

.....

.....

Kodi mumamva bwanji mumtima mwanu mukamaganizira za Baibulo, lomwe ndi mphatso yamtengo wapatali imene Yehova anatipatsa?

.....

.....

.....

.....



www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

## 3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA WANENA KUTI . . .

**Anthu ndi amene analemba Baibulo.**

MUNGAYANKHE KUTI . . .

**Ndi zoona kuti anthu pafupifupi 40 analemba nawo Baibulo. Koma ndikukhulupirira kuti iwowo ankalemba zimene Mulungu ankawauza, chifukwa . . .**

.....

.....

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

.....

N'chifukwa chiyani mumakonda lemba limenelo?

.....

NGATI WINA WANENA KUTI . . .

**Baibulo linalembedwa kale kwambiri ndipo ndi losathandiza masiku ano.**

MUNGAYANKHE KUTI . . .

**Anthu ambiri amagwirizana ndi maganizo amenewa. Koma ineyo sindigwirizana ndi maganizo amenewa chifukwa . . .**

.....

.....

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

.....

N'chifukwa chiyani mumakonda lemba limenelo?

.....



www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania